

Kuteteza mbozi ndi matenda ku mbeu ndi kupanga kasinthisintha.


Kuteteza mbozi ndi matenda

Mbozi ndi matenda zimachepetsa zokolola ndipo sizimaoneka bwino. Mankhwala atha kugwiritsidwa ntchito koma ndiokwera mtengo ndiponso ndiopsy. Njira zina zotetezela mbozi ndi matenda ndi izi:

- Kugwiritsa ntchito mbeu zamakono
- Kutsatira njira zoyenera za ulimi (kuthira feteleza, kupalira ndi kuthilira)
- Kasinthisintha wa malo
- Kulima mozungulira malo amene mwabzalapo mbeu.
- Kuyendera munda pafupipafupi kuona ngati m'munda muli mbozi kapena matenda kuti njira yofuna kuthana nazo ipezeke nsanga.
- Pogwiritsa ntchito ombwe ngati mankhwala oteteza mbozi.
- Kasakaniza wa mbeu: mbozi zina zingalewedwe pobzala mbeu zosiyanasiyana za masamba pa bedi limodzi. *Mwachitsanzo*: kubzala anyezi kapena adio kuzungulira phwetekere kumachepetsa bvuto la akangaude afiira.

Kasinthisintha wa malo

Kasinthisintha malo obzalapo mbeu zosiyanasiyana m'nyengo iri yonse. Izi zimachepetsa kuchulukana kwa mbozi ndi matenda amene amapezeka mbeu zofanana ndipo zimathandiza kusunga chonde mnthaka.



Gawo loyamba: La fodya - phwetekere, mabilingano, tsabola

Gawo lachiwiri: Zamasamba - kabichi, tchainizi

Gawo lachitatu: La mizu ndi nyemba - anyezi, adio, karoti ndi nyemba

Gawo lachinai: La maungu ndi chimanga - nkha, mabvembe, chimanga


Chitsanzo cha

kasinthisintha wa malo:



Ulimi wothilira wa alimi ang'onoang'ono

CHICHEWA



February 2010

Laurence Mathieu-Colas

Goulven Le Bahers

Translation : Mr. Laston M. Makina

This document has been produced with the financial assistance of the European Union. The contents of this document are the sole responsibility of Inter Aide and can under no circumstances be regarded as reflecting the position of the European Union.

KUFOTOKOZA

Kodi kuthilira n'chiani?

M'dera luma ndi mnyengo ya dzuwa, chinyonho chingakhale chosakwanira kulima mbeu.

Pa zifukwa zimenezi, madzi atha kuthiridwa m'minda pofuna kusunga chinyonho m'nthaka kuti ulimi uchitike: uku ndiko kuthilira.

Kuthira madzi pa chigawo cha munda kungachitike; zikomo chifukwa cha mipope, chokoka madzi choponda ndi ngalande... Molingana ndikupezeka kwa madzi.

M'nyengo ya dzuwa, ulimi wothilira ndi njira yokhayo yopezera zokolola. Izi zimachulukitsa zokolola, choncho zimaonjezera pa zokolola za kumunda.

Izi zimapangisa alimi kukwaniritsa zolinga zitatu:

☞ Kulimbana ndi njala

☞ Kupititsa patsogolo chakudya chofunika mthupi kudzera mu ulimi wa ndiwo za masamba.



☞ Kuchulukitsa chuma ndi kupititsa patsogolo umoyo pogulitsa zokolola zina.



Kupalira ndi kuthira feteleza

Kupalira

Palirani mbeu. Kulimbirana chakudya kwa udzu ndi mbeu kumachepetsa zokolola.

Kuchotsa mphukira (kutengulira) kumapangisa kuti mbeu zibereke zipatso zikuluzikulu ndi zamaonekedwe abwino. Izi ndizofunika makamaka ku chimanga ndi phwetekere.

Kuthira feteleza

Mutha kugwiritsa ntchito kompositi/manyowa ndi feteleza. Kumbukirani kuti manyowa angathandize kuti feteleza agwire bwino ntchito yache ndiponso kuchepetsa kuchuluka kwa feteleza amene angafunike.


Kagwiritsidwe ka manyowa: Sakanizani ndowa ziwiri za kompositi kapena manyowa mchigaulo chiri chonse musanabzale. Njira yina yoyenera kuchita ndikubzala mitengo yobweretsa chonde mnthaka (Ombwe, Gilisidia, Nsangu).

Kagwiritsidwe ka feteleza:

Gwiritsani ntchito D-Compound (kapena 23/21/0+4S) wokulitsa. Thirani patapita masiku atatu kapena anai mbeu zikamera kapena kuokeredwa.



Gwiritsani ntchito CAN ngati wobereketsa. Thirani patapita masabata atatu mutabzala kapena kuokera ndiponso pakapita masabata awiri.



Kuthilira

Ndondomeko zakathiliridwe

Ziri mmusizi ndi zotsogolera zongoyerekeza. Chotsogolera chabwino ndi kuona nthaka ndi mbeu.

Nthawi yobzaka kapena kuokera	Mtudu wa mbeu	Usinkhu*	Mathiliridwe (masiku)
Nyengo yodzidzira (Kuyambira April kufika July)	Zamasamba zomwe sizingapilire (anyezi, tsabola)	Kuyambira pachiyambi	3
		Pamene zikulula	4-5
		Pakati ndi mapeto a nyengo	3-4
	Zamasamba zomwe zingapilira (phwetekere, kabichi, repu)	Kuyambira pachiyambi	4-5
		Pamene zikulula	7-8
		Pakati ndi mapeto a nyengo	7
	Chimanga chachiwisi	Kuyambira pachiyambi	6-8
		Pamene zikulula	9-11
		Pakati ndi mapeto a nyengo	6-8
Nyengo yothenta (Kuyambira August kufika November)	Zamasamba zomwe sizingapilire (anyezi, tsabola)	Kuyambira pachiyambi	2-3
		Pamene zikulula	3-4
		Pakati ndi mapeto a nyengo	3
	Zamasamba zomwe zingapilira (phwetekere, kabichi, repu)	Kuyambira pachiyambi	4-5
		Pamene zikulula	5
		Pakati ndi mapeto a nyengo	4
	Chimanga chachiwisi	Kuyambira pachiyambi	5-7
		Pamene zikulula	5-7
		Pakati ndi mapeto a nyengo	4-6

*Misinkhu ya makulidwe ikuyanganira ndi:

Kuyambira pachiyambi: kumera mpaka kukula;

Pamene zikulula: kufika pamene mbeu zakula;

Pakati ndi mapeto a nyengo: kuyambira kupanga maluwa mpaka kukhwima.

Kodi tingakonze bwanji ndondomeko ya zokolola?

Ngati alimi sakonza bwino ndondomeko ya zokolola, zokolola zao zonsa zingapite pa nsika nthawi imodzi ndi anzawo ndipo malonda azabvuta (osapundula, mtengo wotsika).

Choncho, ntchito isanayambike, alimi aganizire mozama pa zambeu zomwe angalime ndipo nanga ndi mwezi wanji womwe angayambe.

Kodi ndibzale chiani?

Chisankho cha mbeu zoyenera kubzala chizadalira pa zomwe alimi afuna kuzadya ndi zimene afuna kuzagulitsa.

Pa mbeu zofuna kugulitsa, alimi aganizire za kupezeka kwa msika:

- Ndi msika uti womwe angapite mosabvutikira mayendedwe?
- Pa nsika uli onse, nanga ndi mbeu iti ingathamangiridwe (ogula ochuluka)?
- Pa nsika uli onse, nanga ndi mbeu iti yomwe ingagulitsidwe pa mtengo wabwino (*mwa chitsanzo, ngati aliyense agulitsa phwetekere, mtengo umakhala wotsika ndipo ndibwino kusankha mbeu yina*)?

Kodi tiyambe liti?

Alimi aganizire za nyengo yabwino kugulitsa mbeu kuti apende nyengo yabwino yoyambira kufetsa njere.

Kunena za masamba, alimi asamalitse: ngati angafetse zonse nthawi imodzi azakolola zonse nthawi imodzi ndipo kuzakhala kobvuta kugulitsa. Choncho n'kwabwino kufetsa pang'onopang'ono kuti zokolola zikhale mnyengo yonse.


Kukolola kawiri, kumene kuli madzi, kumapangitsa kukolola zochuluka ndipo kumathandiza kupeza mitengo yabwino.

KULIMA MOBZALA MBEU

Malo akonzedwe nsanga isanafike nthawi yobzala mbeu potsatira ndondomeko izi:

Kupanga khwawa lalikulu ndi makwawa ogawa madzi

1- Lembererani khwawa lalikulu ndi khwawa logawa madzi pogwiritsa ntchito zikhomo ndi ludzi. Makwawa atambalale 30cm, ndipo mkati mwa makwawa mukhale malo okula 3m.



2- Pangani mzera wa khwawa lalikulu wokwera 30cm, ndipo ulondole chingwe.



Kuthilira

c) Mtundu wa mbeu ndi makhalidwe ache

Kuchuluka kwa madzi ndi ndondomeko yakathiliridwe zimadalira pa zinthu zingapo:

Kukula kwa mbeu: Pamene mbeu ikukula, imafuna madzi ochuluka. Choncho mbeu imafuna kuthiliridwa kawirikawiri koma ndi madzi ochepa ikadali yaing'ono ndipo kuchepetsa kuthiliridwe koma ndi madzi ochuluka pamene ikukula.

Makulidwe: Pamene mbeu zikufika pa nsinkhu wina, kuchepa kwa madzi kungaononge zokolola.

Ndibwino kuonetsetsa mbeu zikuthiliridwa mokwanira mnthawi imeneyi.

Mbeu	Misinkhu yofuna madzi kwambiri
Kabichi	Kufunga ndi kukhwima
Chimanga	Kumasula ndi kuika maso
Anyezi	Pamene akuika
Mbatatesi	Kuphuka, kuika ndi kukhwima
Phwetekere	Kuyamba maluwa mpaka kukolola

d) Mlimi azionesetsa pafupipafupi


Njira yabwino ndiyoti mlimi aziyang'ana mbeu ndi nthaka m'mene zikuonekera kuti athe kudziwa kuchuluka kwa madzi amene akufunika.

- Maonekedwe a mbeu: Kusintha mtundu kwa masamba (kubiriwira motuwa) kapena kufota ku mmawa kapena mazulo, apa mpozizikiratu kuti mbeu ikufuna madzi.
- Maonekedwe a nthaka: Tengani dothe pang'ono (osati lapa mwamba). Kupatula nthaka yamchenga, ngati nthakayo singaundike, muyenera kuthilira.
- Kagwedwe ka mvula: Onani m'mene madzi amvula alowera mnthaka; ngati mupeze kuti madzi sanalowe mokwanira, pitirizani kuthilira monga umo zifunikira.

Kuthilira

Cholinga chothilira ndi kupereka madzi okwanira ofunika ku mbeu kuti zikule bwino.

Momwe tingadziwire kuchuluka kwa madzi amene tingathire?



a) Maonekedwe a nthaka

Mtundu wa nthaka umaonetsa mmene madzi akuyendera mnthaka.

Ndi kuchuluka kwa madzi amene angagwire ntchito ku mbeu. Madzi amalowa mofulumira mnthaka ya mchenga koma sasungika ngati mnthaka ya makande. Choncho nthaka ya mchenga imafuna madzi ochepa koma kuthilira kawirikawiri kutsiyana ndi m'makande.

b) Nyengo

Mbeu zimafuna kuthilira pang'ono mnyengo yodzidzira kutsiyana ndi mnyengo yotentha.

Chofunika ku mbeu zambiri ndi kuthilira:


- Kwa masiku 5 kapena 7 alionse mnyengo yodzidzira (kuyambira April mpaka July)
- Kwa masiku 3 kapena 5 alionse mnyengo yotentha (kuyambira August mpaka December)

kapangidwe ka khwawa lalikulu ndi makwana ogawa madzi

3- Pangani khwawa pamwamba pa nzera. Ngati simugwiritsa ntchito chokoka madzi choponda, mungopanga nzera osatsendera ndipo osapanga khwawa.




4- Thirani madzi ndi kutsendera khwawa lalikulu.



Kupanga zigawo

5- Kujambula zigawo pogwiritsa ntchito zikhomo ndi chingwe. Zigawo zikule 3m mulitali 1.2 mulifupi ndi mpata wa 30cm pakati pao popanga mizera.



6- Kupanga chigawo: pangani mzera ndi khasu. Mukatero ikani manyowa okwanira ndowa ziwiri ndipo tipulirani mchigawocho 30cm kuzama kwache.




Kubzala

Kuokera mbande

1. Wokerani mbande kummawa kapena madzulo pofuna kuchepetsa kuchoka kwa madzi mmbande kudzera mu mpweya. Thirani madzi pa nazale ndipo dikirani kwa ora limodzi musanawokere.

2. Dzulani mbande imodzi imodzi ndipo midzu ikhale ndi dothe la pa nazale.

3. Tengerani mbande mu ndowa, dengu kapena chotengera cha malo okwanira. Lekanitsani mbande zomwe mizu yake yalukana mosamala.



4. Kumbani dzenje lakuya 3-4 cm. Yikani mbande pa dzenje mosamala ndipo midzu iyang'ane pansi.


5. Tsenderani dothe ndi zala kuzungulira mmene munalekezera dothe la kunazale kuti mbande iime bwino ndi kuchotsa mpweya mu dzenje.



Kubzala

Mbeu monga chimanga, therere ndi mbatatesi zikangobzalidwa pamalo pake.

Pangani mapando mmalo m'mene munaika chizindikiro, ikani mbeu m'maenje ndipo kwirirani ndi dothe.



KUSAMALIRA MBEU

Kupanga zigawo ndi kutalikirana kwa mbeu

Kukonza malo obzalapo mbeu

Musanabzale mbeu mzigawo chitani izi:

- Thirani ndowa ziwiri za manyowa kapena kompositi mchigawo chiri chonse ndikutembenuza mozama 30 cm.
- Onetsetsani kuti zigawozo ndizotsalaza bwino.
- Thirani madzi mzigawo ndipo papite ora limodzi musanabzale/kuokera.

Kutalikirana kwa mbeu koyenera

	Kutalikirana kwa mizera	Kutalikirana kwa mapando
Phwetekere	90 cm	60 cm
Kabichi	70 cm	60 cm
Therere*	90 cm	45 cm
Anyezi	30 cm	10 cm
Mpiru	45 cm	45 cm
Repu	45 cm	45 cm
Mapiringano	90 cm	75 cm
Kachewere/Mbatatesi	20 cm	30-40 cm
Chimanga chamakono*	75 cm	25 cm

* Kubzala: Therere (mbeu ziwiri pa phando, kuzama kwa dzenje 2.5 cm)
Chimanga (mbeu imodzi pa phando, kuzama kwa dzenje 3-5 cm)


Yikani zizindikiro mmapando moyenera musanabzale, pogwiritsa ntchito miyezo ya mitengo ndi zikhomo.

Kupanga zigawo

7- Saladzani zigawo pogwiritsa ntchito madzi ngati chokulondolerani.




8- Malo omalizidwa kukonza.



Kuthilira malo pogwiritsa ntchito chokoka madzi choponda


1- Mlimi A akuthira madzi mofikira ndi kunyamula paipi yopereka madzi.

Mlimi B akugwira kothera kwa paipi yokoka madzi mpaka itazaza ndikuona kuti mulibe mpweya.



2- Mlimi B watsiya paipi yokoka madzi mmadzi.

Mlimi A watsiya paipi yopereka madzi ndikuyamba kupalasa chokoka madzi.




3- Tenganani paipi yopereka madzi kuchoka kuchokokera mpaka kofikira madzi. Limbitsani ndi timitengo kumapeto a paipi kuti isachoke.


4- Thirani dothe mmatumba ang'ono a pulasitiki agwire ntchito yotchinga ndi kupititsa madzi mbali ina.

Dzadzani chigowo chimodzi chimodzi.


Sinthani malo a thumba la pulasitiki pamene chigawo chadzadza ndi madzi.



Kudzulira, kupatulira, kukhwimitsa mbande




7- Pitirizani kuthilira kawiri pa tsiku. Mthunzi uchotsedwe pakatha masabata awiri ndipo muzithilira kamodzi pa tsiku. Patulirani mbande pa nazale, ndi kutsiya zina zatalikirana 6 cm. Onetsetsani kuti palibe udzu pa nazale.




8- Wokerani mbande zikafika pa nsinkhu wa 10-15 . Chepetseni kathiliridwe patangotsala sabata imodzi kuti muokere.

Kuthilira ndi kuika mthunzi




5- Pitirizani kuthilira kawiri pa tsiku.



6- Udzu wophimbira bedi uchotsedwe pamene njere zamera ndi kupanga mthunzi wokwera 30 cm.

KUSAMALA NAZALE



Manazale amakhala ndi zofunika kupanga mbeu za mphamvu ndi thanzi zomwe zingakule bwino zikaokeredwa, chifukwa mbeu zochuluka zingasamalidwe mosavuta pa malo ochepa, a chonde ndi otetezedwa bwino.


Mbeu zoyenera kufetsedwa ku nazale ndi izi: phwetekere, anyezi, mapiringano, kabichi, mpiru ndi repu.

Kusankha malo


Malo abwino a nazale ayenera kukhala:

- Malo a chidikha popewa kukokoloka kwa nthaka
- Asakhale pa mthunzi wa mitengo
- Pafupi ndi madzi popeza mbande zimafuna kuthiliridwa
- Nthaka ya chonde, yolowa madzi pang'onopang'ono
- Malo otetezedwa ku ziweto

Kukonza bedi




1- Pangani bedi lokwera 20 cm, 1 m muling'ono ndi 3-4 m mulitali. Thirani madzi bwinobwino ndi kudikira kwa ora limodzi musanafese njere.




2- Lembani mizera yakuya 0.5 cm yotalikirana 20 cm kuchoka pa nzera kufika pa wina ndipo muikemo mchenga.

Kufetsa ndi kuphimbira



3- Fetsani njere imodzi imodzi mmizere ndipo zitalikirane 3 cm ndipo kwirirani ndi dothe ndi mchenga.



4- Phimbirani ndi udzu wopaza bwino ndi wouma ndipo thirani madzi pa bedi.